# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA NKHOTAKOTA M'DZINJA LA 2025-2026

## DZINJA LA 2025/2026 MWACHIDULE

Katenthedwe ka Nyanja ya mchere ya pacific sikakhudza kwambiri nyengo ya dzinja ya 2025/2026.

Boma la Nkhotakota likuyembekezeka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposera apo munyengo ya dzinja ya 2025/2026.


## October 2025




Boma la Nkhotakota kudzakhala kopanda mvula mwezi wa October kupatula madera ochepa amene akuyembekezeka kudzalandira mvula yochepera mlingo wa 10mm.

Mphepo ya mphamvu ndi ya mkuntho ikuyembekezeka m'mweziwu.


## November 2025




Mwezi wa November,nyengo yopanda mvula ikuyembekezeka kupitilila m'madera ambiri m'bomali, komabe madera ena adzalandila mvula ya mlingo wa pakati pa 20mm mpakana 50mm.

Mphepo ya mphamvu ndi ya mkuntho ikuyembekezereka m'mweziwu.


## December 2025




Mvula yokhazikika ikuyembezeka kugwa kuyambila sabata la chitatu la mwezi wa December 2025.

Madera a TA Kafuzila, Nkhotakota Game Reserve ndi Nkhotakota Boma akuyembekezeka kudzalandila mvula yoposela mlingo wa 200mm pomwe madela onse a m'bomali akuyembekezeka kudzalandila mvula ya mlingo wapakati pa 100 ndi 200mm omwe uli mlingo wokhazikika.

## January 2026





Mwezi wa January , boma la Nkhotakota likuyembekezera kudzalandila mlingo wa mvula okhazikika kapena kuposera apo, ndipo madera ambiri adzalandira mvula yoposera 250mm. Koma madera ena a TA Kanyenda ndi mbali zina za Nkhotakota Game Reserve ayembekezere kudzalandira mvula yamlingo wochepera 200mm.

Ng'amba ya masiku osaposera asanu ndi awiri ikhoza kudzakhalako m'madera ena.

Pali chiopsyezo chakusefukira kwa madzi.

## February 2026





Madera ambiri a m'bomali akuyembekezereka kudzalandila mlingo wa mvula yapakati pa 150mm ndi 200mm.

Madera ena amwa SC Mphonde ndi Nkhotakota Boma adzalandila mlingo wa mvula yokwanira 250mm.Milingo imeneyi ndiyokhazikika kapena kuposera apo.

Ng'amba yosaposera sabata imodzi ikuyembekezeka.

## March 2026





Mvula ya mlingo wokhazikika komanso oposera apo ikuyembekezereka m'bomali.

Madera ambiri akuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wapakati pa 200 ndi 300mm. Koma Nkhotakota Boma ndi madera ena a TA Mphonde akuyembekezereka kudzalandira mvula ya mlingo oposera 300mm.

Pali chiopsyezo chakusefukira kwa madzi m'madera amene amakhuzidwa ndi madzi osefukira.

## April 2026





Nyengo ya dzinja mu boma la Nkhotakota ikuyembekezeka kudzatha Kumapeto a mwezi wa April 2026 .

Mlingo wa mvula yonse umene madera ambiri akuyembekezereka kudzalandila munyengoyi ndi kuyambila 40 mpakana 100mm. Pamene madera a apo ndi apo ozungulira boma la Nkhotakota adzalandila mvula ya mlingo okwana 150mm.

Boma la Nkhotakota likuyembekezeka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposera apo munyengo ya dzinja ya 2025/2026. Mvula yokhazikika ikuyembezeka kugwa kuyambila sabata la chitatu la mwezi wa December 2025. Nyengo ya dzinja ikuyembekezeka kukhala ya masiku pafupi fupi 130 mpakana 140. Nyengo ya dzinja mu boma la Nkhotakota ikuyembekezeka kudzatha Kumapeto a mwezi wa April 2026 . Ng'amba yosapitilila sabata imodzi ikuyembekezeka mwezi wa January ndi Febraury.

| NKHOTAKOTA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 0.1 | 4.4 | 7.5 |
| NOV | 15.9 | 62.0 | 21.9 |
| DEC | 181.8 | 244.9 | 151.4 |
| JAN | 232.5 | 349.1 | 203.5 |
| FEB | 190.5 | 295.2 | 240.6 |
| MAR | 271.4 | 401.4 | 322.0 |
| APR | 84.4 | 125.9 | 150.8 |




**Ulosiwu udzaunikidwanso mu mwezi wa December 2025**


**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw



Zapangidwa ndi kusindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: